

JOYCE
MEYER

MTENDERE

NDI KUTAYA PA LYE NKHAWA YANU YONSE,

PAKUTI LYE ASAMALIRA

Unless otherwise indicated, all Scripture quotations are taken from
THE AMPLIFIED BIBLE: Old Testament.

Copyright © 1962, 1964 by Zondervan Publishing House
(used by permission); THE KING JAMES VERSION; and from
THE AMPLIFIED NEW TESTAMENT
Copyright © 1958 by the Lockman Foundation
(used by permission).

Copyright © 2014 by Joyce Meyer Ministries – South Africa

All rights reserved. No part of this publication may be
reproduced, distributed, or transmitted in any form or by any means,
or stored in a database or retrieval system, without the prior written
permission of Joyce Meyer Ministries – South Africa.

Joyce Meyer Ministries – South Africa
PO Box 5, Cape Town, 8000

Phone: +27 (0) 21 701 1056
Website: www.joycemeyer.org

Go to tv.joycemeyer.org to watch Joyce's messages in a
variety of languages

Peace – Chewa
Not For Resale

ZA MKATI MWA BUKULI



<i>Mau Oyamba</i>	4
1. Kodi Mukusangalatsidwa Ndi Mtendere	5
2. M'mene Mungasangalalire pa Mtendere	7
3. Mutsogozedwe Ndi Mtendere	10
4. Ndi Zinthu Zotani Zimene Zimakuberani Mtendere Wanu Kodi?	13
5. Chifukwa Chiani M'dyerekezi Amakuberani Mtendere Wanu?	16
6. Maimidwe A Okhulupirira Mu Nthawi Ya Mayesero	22
7. Kulitenga Tsiku Liri Lonse M'mene Liliri	26
8. Pemphereo Limadzetsa Mtendere	30
Pemphero La Chipulumutso	33
Za Olemba Bukhuli	34

MAU OYAMBA



“....Afunefune mtendere (mgwirizano; kusasokonezeka ndi mantha, zokhumba zogwedezeka, ndi kutsutsana kwa chikhalidwe) ndi kuulondola. (Osangokhumba kokha ubale wa mtendere ndi Mulungu basi, anthu anzathu, ndi iwe mwini, koma uwatsate iwo ndithu!)”

I Petro 3 ndime 11 (AMP)

Ndikupemphera kuti buku ili la mtendere likuthandizani inu kuphunzira kumasangalala “.....mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse....”

Afilipi 4 ndime 7

1



KODI MUKUSANGALATSIDWA NDI MTENDERE

Mwana aliyense wa Mulungu obadwanso kwa tsopano ayenera kumasangalala ndi moyo wodzazidwa ndi mtendere. Yesu anati pa Yohane 14 ndime 27 (AMP):

“Mtendere ndikusiyirani inu, mtendere wanga ndikupatsani; Ine sindikupatsani monga dziko lapansi lipatsa. Mtima wanu usavutike, kapena usachite mantha. (Siyani kudzilolera inu nokha kugwedezeke ndi kusokonezeke; ndipo musapereke mpata kwa inu eni kuti mukhale amantha ndipo onyozedwa ndinso osalimba mtima kapena osakhazikika.)”

Awa ndi Mau a Mulungu a mphamvu kwambiri. Chonde muwawerenge kangapo, kenako mutenge mphindi zosachepera zisanu kuwalingalira iwo mupemphero ndi kuwalola kuti akhazikike mkati mwanu.

Poyamba tiyeni tizindikire kuti mtendere umene Yesu amapereka ndi mtendere wapadera, osati ngati umene dziko limapereka. Kodi mtendere umene dziko limapereka ndi otani? Dziko limapereka mtendere womvekera mwa mtundu wina wake. Mtendere umenewu umagwira ntchito pamene china chiri chonse m'moyo mwanu chikuyenda mu njira imene inuyo mukufunira. Komatu, pamene zinthu sizikuyenda mu njira yomwe tikufuna, mtendere wa m'dziko umenewu umatha mwachangu zedi. Ndipo mzimu “okhumudwa”

umalowa m'malo mwake mwansanga ndithu. Mtendere umene Yesu amapereka umapezeka pa nthawi yabwino ngakhalenso pa nthawi yovuta, pamene tiri ndi zinthu zochuluka ngakhalenso tikachepekedwa. Mtendere wake umagwira ntchito pakati-kati pa mafunde.

Zikanakhala zokoma, m'mene moyo waku thupi uliri, ngati zonse zikanamayenda mu njira yomwe tikufunira nthawi zonse. Tikudziwa ndi m'mene zinthu zimakhallira kuti izitu sizimachitika konse ai. Ngati okhulupirira, ineyo ndinayesetsa kugwiritsa chikhulupiriro changa kuchotsa china chiri chonse chomwe sichimandikondweretsa komanso chimene sindimamvacho bwino konse. Izi zinandipangitsa kukhumudwa kwakukulu zedi. Ukamayesera kuchipangitsa china chake kuti chichitike chimene sichingachitike ndipo sichingadzatheke zimakhumudwitsatu nthawi zonse. Nditazindikira kudziwa Mulungu, ndinayamba tsopano kuzindikira kuti ndinafunikira kugwiritsa ntchito chikhulupiriro changa kuti ndidutse mwa bata ndi mtendere mafunde ndi mayesero a moyo. Ndinafunika kusiya kumamulola m'dyerekezi kumandibera mtendere wanga nthawi zonse ndikazunguzika.

Yesu anati pa Yohane 14 ndime 27 (AMP), *“Mtima wanu usavutike, kapena usachite mantha.”* Pamene ndi nkawerengawerenga *Mau a m'Buku Lopatulika amenewa ndikumawalingalira, ndinkazindikira kwambiri Baibulo likundiiza ineyo kuti zimenezizo zikundichitikira ine mwini. Ndipo ndinafunika kusiya zimenezo. Iye anatinso mu ndime yomweyo, “Musalole kuti mitima yanu ivutike, kapenanso kuti ichite mantha”*

Yesu anawadzudzula ophunzira ake pa Marko 4 ndime 40 chifukwa chosowa chikhulupiriro kotero kuti mtendere wawo unatayika mu mafunde aja. Yesu sanataye mtendere Wake ai. Anali ali chigonere kumbuyo kwa ngalawa. Ophunzirawo anapanikizika ndi kukhumudwiratu.

Kodi nanga inu mukadamva bwanji? Mukanakhala kumbuyo kwa ngalawa ndikumasangalala mumtendere ndi Yesu? Ngatitu inu mulibe mtendere simukusangalala ndi moyowu ai.

2



M'MENE MUNGASANGALALIRE PA MTENDERE

Palibe uthenga umene ungapindule pokha-pokha ndondomeko zitaperekedwa za m'mene “ungathekere” ndiponso m'mene ungaperezere zinthu zomwe iwe ukufunazo. Kunena kuti ukufuna mtendere imeneyo ndi ndime yoyamba. Komabe, popanda kugawana kogwirika bwino kwa m'mene mungakhalire nawo mtenderewo, mphotho yeni-yeni siingaonekere.

Chinthu chimodzi chinandithandiza ine kwambiri zedi ndi kuyamba kumasangalala ndi moyo wa mtendere. Ndinazindikira kusafunikira ndi kudzivutitsa kwambiri kwake “komayesera kupanga china chake chomwe sindikanakwaniritsa kuchichita mwa ine ndekha.” Kodi inu mukuchita zotero? Kungodzivutitsa nokha kumayesera kuzipangitsa zinthu kuti zichitike? Mulungu ali ndi nyengo yoyenerera zedi ya chinthu chiri chonse. Mukuyenera kuyembekezera pa nyengo Yake.

Kweni-kweni, simungathe kuzipangitsa zinthu kuti zichitike nyengo yake isanakwanetu. Ngakhale mutabadwitsa chinthu china chake nyengo yake isanakwane, inutu simudzakhala ndi chimwemwe ndi icho ai. Phunzirani inu kuyembekezera pa Mulungu. Izi zimamubweretsera Iye ulemu, ndipo zimakubweretserani inuyo mtendere.

Kodi mukuyesera kuchitachinthu chosatheka? Mukuyesera kuwasinthanthu omwe akuzungulirani, mwinatu munthu amene munakwatirana naye, m'modzi mwa ana anu, bwenzi lanu, kapena m'mbale wanu? Anthu sangawasinthanthu anzawo. Ndi Mulungu yekha amene angalowe mkati mwa mtima wa munthu ndikumupangitsa bamboyo kapena mayiyo kusintha. Tikawakamiza anthu ochokera kunja kuti apange zinthu, mapeto ake zimamuchotsera aliyense mtendere. Ifetu sitinalengedwe kuti tiikidwe pansu pa chilamulo ai. Anthu amafuna kumasulidwa. Amafuna mpata wabwino kuti azitakasuka.

Zaka zoyamba zingapo nditangokwatiwa ndinkayesera kumamukamiza mwamuna wanga kuti asiye kusewera masewero a mpira wa gofu. Ndinkangowona ngati amaonjeza maseweredwe ake, koma ineyo ndinkafunitsitsa kumacheza naye limodzi pafupi-pafupi. Ndinayesetsatu njira iyi ndi iyo imene ndikanatha. Ndinayesera nyambo zosiyana-siyana, ndinkakwiya, kuzunguzika, ndikuyesetsa kumamuuzitsa, mpaka kenaka ndinasiya osama muyankhulitsanso. Koma palibe chomwe chinagwira ntchito kundithandiza. Ndinkangokhumudwa nthawi zonse. Mwa kamodzi-kamodzi iye ankatha kusiyadi osakasewera kwa kanthawi ndithu. Tsono choseketsa chake chinali chakuti angakhale chimene ndimachifuna chinakwaniritsidwa, komabe ineyo mtendere ndinalibe. Ndinalibe mtenderechifukwa chakuti ndimayesera kupeza chimene ndimachifuna mu njira yolakwika. Ngati mukumayesera kumukamiza wina wake kuti asinthe, izi zidzakusowetsani inu mtendere.

Kodi mumakhumudwa kwambiri ndi inu mwini chifukwa chakuti simuli pamulingo umene mukufuna kukhala m'moyo wanu wa uzimu? Mukufunika kukhala pa chiyanjano ndi Mzimu Woyera mokhudzana ndi ntchito imene Iye akuchita m'moyo mwanu. Iyetu akukubweretsani inu n'kuyeretsetsa kapena m'kukhwima. Izi simungazichite inuyo panokha ai. Ilinso ndi gawo lina lomayesera kuchita zinthu zina zomwe inu simungazikwaniritse.

Ndikhulupirira mwaona kuti ndi moyo wa chibadwidwe zedi

kumayesera kuchita zinthu kuzisintha zimene inuyo simumazikonda konse. Tatiyeni tinene chilungamo panopa. Kodi inuyo mwayesera kukwaniritsako kuzisintha zinthu zimenezizi? Kapena mungodzivutitsapo nokha basi ndikumangoutaya mtendere wanu pamene mukuyenera kumapuma mwa Mulungu, kumayembekezera pa Iye ndi nyengo Yake, kumukhulupirira Iye pompatsa anthu ena amene ali m'moyo mwanu komanso pamodzi ndi inu eni?

Ine ndingophera mphongo apa pokuuzani ichi: ngati inuyo “mukuyesera kupanga chinthu china chake pa chinthu chomwe inuyo simungathe kuchitapo chiri chonse pa icho” mungodzivutitsa ndipotu simudzasangalala konse ndi mtendere.

3



MUTSOGOZEDWE NDI MTENDERE

Akolose 3 ndime 15 (AMP)

“Ndipo mtendere (mgwirizano umene umadza) wa Khristu uchite ufumu {ukakhale ngati rifali mosalekeza} m’mitima yanu, [kulingalira ndi kukhazikitsa kumapeto pa mafunso onse amene muli kulingalira m’maganizo anu...]”

Rifali mu masewero a mpira amalingalira ngati inu muli mkati kapena kunja. Mtendere ukuyenera kukakhala rifali amene akulingalira ngati chinthu chikuyenera kukakhala mkati mwa moyo wanu kapena kunja.

Anthu ambiri sasangalala ndi mtendere chifukwa chakuti ali kunja kwa chifuniro cha Mulungu. Iwo amatsata chifuniro chawo osati chifuniro cha Mulungu. Iwo amachita zimene akumvetsera ngati kapena kuganizira kuti ndi zolondola osati kutsatira Mau a Mulungu ndi kutsogozedwa ndi mtendere. Nthawi zambiri china chake chikandichitikira chomwe ndikufuna kuti ndichichite. Chimaoneka ngati chinthu chabwino, chimamvekera bwino, komanso chimakhala kuti ndi chinthu chabwino ndithu. Koma, ngati ndilibe mtendere, ndimangochisiyiratu osachichita ai. *Mutsogozedwe ndi mtendere.* Musagule chinthu china chake, maka-maka chinthu cha mtengo waukulu, ngati inuyo mulibe nacho mtendere chinthucho. Ngakhale

muchifune bwanji, mudzamva chisoni ngati muchita motsutsana ndi kutsogozedwa kwa Mzimu Oyera.

Nthawi zinanso ndimakhoza kupatsidwa mwayi okalalikira kwina kwake umene ine ndimaulandira ndithu, koma ichi sindimakhala nacho mtendere ai. Sindikudziwa chifukwa chake kuti n'chiyani ai, koma nthawi zina mtendere sumakhalapo pamenepo ai. Ndinaphunzira kuti ngati ndichivomerebe chimenechi, kumadzabwera kutsogoloko chinthu china chake chimene chimadzandizindikiritsa ineyo chifukwa chake ndikanayenera kutsatira mtendere.

Utumiki wina ndikukumbuka ndi omwe ndinayambirira kuyenda. Mautumiki okalalikira anali apang'ono zedi komanso otalikirana-talikirana nthawi imeneyo. Muchibadwidwe, ndinkakhumba nditavomera kupita konseko. Ndinaitanidwa ku mpingo waku Texas. Chinali chinthu cha mtengo wapatali kwa ineyo pa nthawiyo. Ndipo ndinavomera nthawi yomweyo mosakaikiranso. Patapita milungu ingapo, mumtima mwanga mumakhala kutsutsika nthawi zonse ndikauganizira ulendowo. Kutsutsikaku kumakulira-kulira. Kenako mosakaikiranso ndinalibiretu mtendere kuti ndipiteko, komatu Ambuye sanandipatse chifukwa chake kuti ndi chiyani.

Ndinali kumangoyembekezera-yemembekezerabe, pamapeto pake ndinayenera kuwaimbira telefoni iwo kuti ndiwapemphe kuti angondimasula ku lonjezo lomwe ndinapangana nawo lija. Ine ndinawauza kuti ineyo kumeneko ndidzakatumikirako pokha-pokha ngati iwo sakwanitsa kupeza munthu oyenerera kuti akalalikire m'malo mwanga, koma pazifukwa zina, ine ndinalibetu mtendere kuti ndipiteko. Ndipo iwo anandimasula ku lonjezanolo.

Patangopita milungu ingapo ndinazindikira kuti mpingo wakwathu unali ndi mwambo oyikiza nyumba yatsopano yomwe inamangidwa kumapeto a sabata lomwelo limene ndikanakhala nditapita kukatumikira kumene kujako. Ndinakhala othandizira Abusa ku mpingo umenewu kwa nthawi ndithu ndisanayambe utumiki

wangawu, ndipo kunali kofunikira zedi kuti ineyo ndikhale nawo pamodzi panthawi yapadera imeneyo ndithu.

Kodi nanga ndi chifukwa chiani Ambuye sanangondiuzza chimene chimachitika nthawiyo? Pa zifukwa zina, Iye anaona kuti sikunali kofunikira kutero. Mau ake akuti titsogozedwe ndi mtendere. Nthawi zambiri Iye amangokupatsani zoterozo kuti akudziwitseni ngati muli “mkati” kapena “kunja” kwa chifuniro Chake. Mudzadziwa m’tsogolo mwake chifukwa chake, komanso mwina simungadzadziwenso.

Inu simudzakhala ndi moyo wosangalala ngati simumvetsera kutsogozedwa Kwake ndi kutsata chifuniro cha inu nokha.

4



NDI ZINTHU ZOTANI ZIMENE ZIMAKUBERANI MTENDERE WANU KODI?

Zinthu zina ndi zina zimasowetsa mtendere wina aliyense payekha-payekha. Satana wakitengerani moyo wanu onse kukuphunzirani inuyo. Mwinanso ndikutheka ndithu kuti amakudziwani inuyo bwino lomwe kuposera m'mene inuyo eni ake mumazidziwira nokha. Iyeyo amadziwa chimene chimakuvutitsani inuyo. Mukuyenera kuchidziwa chinthu chimene chimakuvutitsani inuyo, ndipo musamalire mu nyengo zotere kuti musautaye mtendere wanu.

“Zinthu zimene zimamubera mtendere” wina aliyense sizofanana-fanana ai. Palitu zinthu zimene zimandivutitsa zimene sizimamuvutitsa konse mwamuna wanga ai. Mwa chitsanzo, ine ndimakonda pamalo pachete, koma iyeyo samakhala ovutitsidwa ndi phokoso ai. Iyeyo amakhoza kumawerenga buku pamene mwana wathu wamkazi ali ndi wailesi yake yatepi itatsegulidwa mokweza zedi komanso mwana wathu wa mwamuna wa zaka zisanu ndi zinayi akumadzigubuduza pansu ndi galu wathu.

Sinditha kukwaniritsa kuchita zinthu mwansanga-nsanga, komanso ndimadana ndi kucheredwa. Nthawi zina mwamuna wanga amayesetsa

kupanga zinthu zambiri-mbiri mukanthawi kochepa. Pamapeto pake zimatheka kuchita zinthu mwachangu chachikulu zedi kutsilizitsa mumphindi zotsalira pang'ono-ng'ono kweni-kweni. Ichi ndi chinthu china chake chimene mdyerekeziyo amachidziwa mwa ine, ndipo iyeyo amachigwiritsa ntchito ichi kuyesera kundibera mtendere wanga. Pamene mwamuna wanga mbali inayi, akufuna kuti azikafika ku bwalo la ndege munthawi yolawira kosachepera ola limodzi tikamapita kokakwera ndege kupita kwina kwake. Iyeyo amafuna kumakafika kumalo kosewerera mpira wa gofu molawilirakobe akamapita kokasewera masewera a gofuwo. Ngati m'dyerekezi akangoyesera kumutsogolera iyeyo kuti acheledwe kukafika ku ena mwa amodzi mwa masewero akewo, mwamuna wanga amasoweratu mtendere .

Ndife osiyanatu, choncho, satana amagwiritsa ntchito tinjira tosiyasiyana mwa wina aliynense wa ife. Khalanitu atcheru woposa iyeyo. Iyeyo amakutcheranitu kuti akusokonezeni. Kodi “zinthu zimene zimakuberani mtendere” wanu ndi zotani? Lembani ndondomeko ya izo ndikukambirana ndi banja lanu lonse. Pezani zimene zimawaiipira iwo kwambiri, ndipo yeserani kuthandizana wina ndi mnzake kupewa madera amenewa.

Mwamuna wanga ndi osewera mpira wa gofu modzipereka kwathuthu zedi. Ine ndimasewera, koma zimandiyenerenza bwino kumaseka ndi phokoso ndikumangozungulira pa bwalo lake losewelerapo. Koma ine ndaphunziratu, kuti sichinthu chanzeru kuti ndizikasokoneza-sokoneza kwambiri pamene ineyo ndiri kumasewera naye mwamuna wangayo masewera a mpira wa gofuwo mwinanso kumamusinjirira iyeyo akaponya mpira molakwika. Nthawiyi imakhala yosangalatsa kwa ife ndithu, koma ndimayenera kuchita mosamalitsa kuti iyeyo ziamukhalirensa bwino naye. Palibe chanzeru chiri chonse chomwe chingapindule pomupangitsa wina wake kuti autaye mtendere wake. Mukakhala ndi munthu wina wake malo amodzi kwa nthawi yaitali, umayamba kumadziwa kufooka kwake pamodzinso ndi kwako komwe. Ndikubwerezanso kuti, “Yesetsani kuthandizana wina ndi

mnzake kupewa madera amenewa.”

Mwamuna wangatu amandithandiza muzofooka zanga. Amayesetsa kundithandiza kuti zinthu zikhale chete pamene ndikuyesera kuti ndiwerenge kapenanso kupuma. Iye amandilimbikitsa kuti ndipume kapena kupeza zochitika zina chifukwa chakuti amadziwa kuti ngati ineyo ndatopa kwambiri. Satana amandibera mtendere wanga. Agalatiya 6 ndime 2 ikuti, (NKJV) *“Nyamuliranani zothodwetsa...”* Timafunikira kunyamulirana zofooka za wina ndi mnzake, pozindikira kuti tiri nazo zambiritu mwa izo komanso kupemphererana wina ndi mnzake.

5



CHIFUKWA CHIANI M'DYEREKEZI AMAKUBERANI MTENDERE WANU?

Tikudziwa kuti mtendere ndi umene umatilumikiza ndi Mzimu Oyera. Munjira ina tikhoza kunena kutinso Mzimu Oyera amagwira ntchito pamene pali podzala ndi mtendere. *Muli mphamvu mu mtendere*. Ine ndikukhulupirira kuti ndi chifukwa chake pa Yohane 14 ndime 27 (AMP) akutiuzwa kuti ulamuliro wathu umene tinalandira wochoka kwa Yesu ndi mtendere. Yesu anati “...*mtendere wanga (wa ine mwini) ndikupatsani; Ine ndikupatsani inu...*” tikhozanso kunena kuti, Iye chifuniro chake ndi mtendere Wake kwa ife.

Ngati muli ndi vuto ndipo m'dyerekezi sakutha kukupangitsani kuti muzunguzike nalo, iyeyo alibe mphamvu ya ulamuliro pa inu. Inu mphamvu yanu ndi yosungitsa bata, mtendere, malingaliro odalilika. Mphamvu za m'dyerekezi ziri mkati mokupangitsani inu kuti musokonezeke ndi mantha.

Pamene inu mupezeka muli muchipsyinjochina chake, inu chotsatira chanu chikhale kungokhala bata basi. Musakadziseweretse nokha m'manja mwa m'dyerekezi podzipangitsa kuti muzunguzike. Iyeyotu amakondwera kuti akupangitseni kuti muzunguzike ndi m'mkwiyo. Nthawi zambiri chinthu choyamba pamene munthu ali mu m'mkwiyo

wake amachichita ndi kunena zinthu kuchokera m'mkamwa mwake zomwe zimamupatsa m'dyerekezi mphamvu zowuonjezera moto omwe iyeyo wangouyatsapo.

Yakobo 3 ndime ya 5 ndi 6 (mu mau ena) ikuti lirime ndi kagawo kakang'ono, koma limatha kuyambitsa moto waukulu. Ndi dziko lauchimo ndithu limene laikika pakati pa magawo athu ena amene akuipitsa ndi kuwononga thupi lonse, ndipo ndi moto oyatsidwa ku gehena. Mukhoza kuona kuchokera ku Mau opatulika a Mulungu kuti m'dyerekezi akufuna inu mutaye dongosolo kuti iye apeze mpata ochita dongosolo lake. Kumbukirani, m'dyerekeziyo amangokuikizani pamalo ndikukupangitsani kuti muzunguzike.

Inu mwina munazindikira kuti m'dyerekezi amagwira ntchito koposera pamene muli kukonzekera kupita ku tchalitchi kokapemphera ngakhalenso kokaphunzira ndi kugawana Mau a m'Baibulo. Kwa zaka zambiri, m'mawa wa tsiku lamulungu liri lonse mkati mwa nyumba yathu mumakhala ngati mwaphulika chithu chachikulu. Sizinkatheka kupita ku tchalitchi popanda wina wa ife kuzunguzika, ndipo kawiri-kawiri amakhala ali wina aliyense wa ife.

Lamulungu m'mawa, zinthu zimangosowa, kutaikira ndi kusweka kuposera tsiku lina liri lonse la sabata imeneyo. Ana athu amakhoza kugwirizana kwambiri mu tsiku lina liri lonse la sabatayo, komatu m'mawa wa la mulungu, amamenyana. Pamene phokoso ndi chipwirikiti chimachulukira-chulukira mu tsikulo, ndi pameneponso ine ndimazunguzika kwambirinso. (Kumbukirani kuti inetu sindikonda phokoso lambiri ai).

Pamapeto pake, ndimayamba kumangodandaula. Mwamuna wanga amadana ndi kudandaula, choncho pakangopita kanthawi, amandiuzwa kuti ndisiye kudandaulako. Ndiye ineyo tsopano ndinkazunguzika ndi iyeyo tsopano. Ndiye ana athu aja amalira chifukwa chakuti ine ndi bambo wawo tikukangana.

Mkati mwa zonsezi, galu wathu amayamba kumangothamanga-thamanga mkati mwa m’nyumba ndi nsapato ya wina wake yomwe akufuna kuti aibvale, ndiye pamenepo ndimayambano kukuwa, “Tamafulumizani, tichedwatu.” Ndikukhulupirira kuti mukutha kuona m’mene zithu zake zimakhallira.

Pamene ndinaona Yakobo 3 ndime 18 ine ndinamvetsano chifukwa chake chomwe izi zimakhala ngati ziri kuchitika pamene tinali kupita kukamva Mau a Mulungu. Mau awa a m’bukhu lopatulika (AMP) “... *kukulola kwa oyera...*” (*machitidwe oyenerera*) “...*ndi (chipatso chake cha mbeu)yodalidwa [Mauwo] “mu mtendere kwa iwo amchitira ndi kupanga mtendere.”*”

Tikhoza kunena kutinso, m’malo moti Mau a Mulungu azikike ndi kubala zipatso zabwino m’miyoyo yathu, akuyenera kuti alalikiridwe kapena kuphuzitsidwa ndi wina wake amene iyeyo ali owupanga-mtenderewo iye yemwe. Komanso, tikufunikira kukhala ndi malingaliro a mtendere pamene timva Mau a Mulungu.

Tangoganizirani za moyo wanu womwe. Ndi kangati kodi pamene m’daniyo wakhala akupambana mumayesero ake kuti atizunguze ife pamenetisananyamukekupitakokamvaMauaMulungu?Kumbukirani kukhala tcheru ku matchera ake, ndipo musasewere m’manja mwake. Akorinto Wachiwiri 2 ndime 11 (AMP) ikunena kuti “*pakuti sitikhala osadziwa*” a satana “*machenjerero ake*” Mu ‘King James’ amati “njira zake.” Satana amagwiritsa ntchito machenjerero ake kutinamiza ndi kutisocheretsa. Tiyeni tikhale ochenjera kumposa m’dyerekeziyo. 1 Petro 5 ndime 8 ikuti (AMP)

“Khalani odzisungira, dikirani; m’dani wanu M’dyerekezi, monga mkango wobuma, ayenda-yenda kufuna-funa wina akamlikwire”

Musalore kuti mukhale inuyo! Ndikukupemphani inu kuti mukhale atcheru. Nthawi zonse pamene mukumva kuti mukufuna kuyamba kuzunguzika kapena kuvutitsika, taimani ndi kudzifunsa nokha

mafunso awa: “Kodi m’dyerekeziyo akufuna kuyesera kuchita chiani? Ndikampatsa malo iyeyo kumalingaliro osakhala bwino amenewa, chotsatira chake chikhala chiani nanga?”

Aefeso 4 ndime ya 26 ndi 27 (AMP) ndi mau a Mulungu a mu Buku Lopatulika ofunikira omwe akutiphuzitsa ife kuti timupewe m’dyerekezi kuti asakakhale ndi gawo mu miyoyo yathu posazunguzika ai. Ndime 26 ikuti “...*dzuwa lisalowe muli chikwiyire (kuipidwa, m’mkwiyo, kapena kuwawidwa).*” Tikhoza kunenanso kuti “Musakhale ozunguzidwa chikhaliire”

Ndime 27 ikuti, (AMP)

“Ndiponso musampatse (ena ali onse) malo m’dyerekezi (kumpatsa mpata iyeyo).”

Pamene mwataya chimwemwe chanu, mumatayanso mphamvu zanu. Nehemiya 8 ndime 10 ikuti “...*pakuti chimwemwe cha Yehova ndicho mphamvu yanu.*” M’salimo la Davide, pa Masalmo 42 ndime 5 NKJV akudziyakhulira iye ku mzimu wake womwe ndipo akuti “*Udziweramiranj... Ndi kuzingwa mkati mwanga?...*” Yesaya 30 ndime 15 ikuti “...*m’kukhala chete ndi m’kukhulupirira mudzakhala mphamvu yanu...*” Tikuonanso kuti m’dyerekeziyonso akufuna kuti asatifatsitse ife kuti atibere mphamvu zathu.

Ndinaphunzira kuchoka kwa Mzimu Oyera kuti amagwira ntchito mumalo amene muli mtendere. Mzimu Oyera sumagwira ntchito mu chisokonezo ai. M’dyerekezi ndi amene amagwira ntchito mu chisokonezo, koma Mzimu Oyera amagwira ntchito mu mtendere. Perekani malo a mtendere m’nyumba mwanu, malo a bizinezi, kumpingo komanso utumiki. Pamene mutero, mudzakhala mukuwalemekeza Mauwo a Mulungu ndiponso Mzimu wa Mulungu. Mudzakolola chipatso cha kukhulupirika kwanu.

Kumbukirani kuti Yesu anatumiza makumi asanu ndi awiri, awiri-awiri mwa iwo kuti akachite zambiri zazikulu: kukatulutsa ziwanda,

kukachiritsa odwala ndiponso kukalalika Uthenga Wabwino. Anawauza kuti apite mu mzinda, akapeza nyumba, akayankhule mtendere kwa iyo ndi kukakhalamo m'menemo. Iwo akakapanda kukalandiridwa (mwamtendere), anayenera kukasasa fumbi la mapazi awo ndi kupitirirapo. (Luka 10 ndime ya 1 mpaka 11, ndi 17) Chifukwa chiani? Ntchito zawo zinali zopanda mphamvu ili yonse pokha-pokha akanakhazikika mu mtendere.

Ndiri ndi chikhulupiriro kuti mukuyamba kulandira bvumbulutso la uthenga wake umene bukuli likufuna kukupatsirani. *Chitani china chiri chonse kuti muyesetse kudziletsa nokha kuti mukhale mu mtendere nthawi zonse.*

Pa Luka 22 ndime 46, (AMP) Yesu akutiphunzitsa ife kupemphera kuti tibatengeredwe kokatiyesa. Anati Iye kwa ophunzira ake, "...Ukani, pempherani kuti mungalowe (konse ai) m'kuyesedwa."

Musadalire mphamvu ya inu nokha kumukana m'dyerekezi mu dera limeneli ai. Pempherani tsiku ndi tsiku kuti Mulungu akupatseni chisomo chomukana m'dyerekezi pamene akuyesera kukuberani mtendere. Mupempheni Ambuye akulimbikitseni inu ndiponso akuthandizeni.

Kumbukirani Yohane 15 ndime 5 (AMP) ikuti "...*Pakuti kopanda Ine simungathe kuchita kathu.*"

Musayesere kuchita mwa inu nokha! Pemphani kuthandizidwa. Mungathe kuchita zonse mwa Khristu (Afilipi 4 Ndime 13) koma osati china chiri chonse mwa inu nokha ai. Pa Yohane 5 ndime 30 (AMP), ngakhale Yesu anati Iye sakanatha kuchita chiri chonse kuchoka mwa Iye yekha. Mukuyenera kukhala ndi malingaliro odzichepetsa ngati mukufuna kuti Mulungu akuthandizeni inuyo. Petro oyamba 5 ndime 5 ikuti (NKJV), "...*pakuti Mulungu akaniza odzikuza, koma apatsa chisomo kwa odzichepetsa.*"

Ndiloleni mwachidule ndinene chonchi kuti satana amafuna kukuberani mtendere wanu kutinso akuberani mphamvu zanu. Akufuna inu mukhale ofooka ndi opanda mphamvu, koma ndikukulimbikitsani inuyo kuti “...*tadzilimbikitsani mwa Ambuye ndi kulimba mwa mphamvu Yake.*” Aefeso 6 ndime 10. Mukhazikikebe mu mtendere!

6



MAIMIDWE A OKHULUPIRIRA MU NTHAWI YA MAYESERO

Aefeso 6 ndime 13 (AMP) ikuti

“...mutachita zonse[zofunikira za zoopsyinja], mudzachirimika [osagwedezeka pa malo panu].”

Kodi “pamalo panu” ndi pati? Aefeso 2 ndime 6 ikutiphuzitsa kuti malo athu ali mwa Yesu. Mau akuti “chirimika” mu chiyankhulo chachi giriki ali ndi liu lakuti “histemi.” Tanthauzo lina ndi lakuti “kukhazikikamo.” Liu la chi giriki la “kukhazikika” pa Yohane 15 ndime 7 ndi “meno.” Tanthauzo linanso ndi lakuti “chirimika.” Ndiye “meno” nthawi zina amatengedwa ndi kumasuliridwa kuti “kuimirira.” Yesu anati *“Ngati mukhala mwa Ine, ndi mau anga akhale mwa inu, pemphani chimene chiri chonse muchifuna, ndipo chidzachitika kwa inu”* Yohane 15 ndime 7 (NKJV). Malo oimidwa ndi malo a mphamvu.

Ahebri 4 akuti pamene mwapuma ku masautso anu, m’ malo mwake kukhale kulimbika (kudzera mu chikhulupiriro ndi kukhulupirika) kuti tilowe mu mpumulo wa Mulungu, ndipo mudzalowa mu mpumulo Wake. Mu nthawi ya mayesero, chitani chimene Mulungu akukutsogolerani kuti muchite, kenako imirirani kapena tengani

malo anu mwa Khristu ndi kumuona Iye akuchita m'malo mwanu. Baibulo likuti "...chirimikani, ndipo penyani chipulumutso cha Yehova" (Eksodo 14 ndime 13) Mau onsewa - kuchirimika, chete, mpumulo, imirira, ndiponso mwa Khristu - akunena chithu chofanana chofunikira: *Musautaye mtendere wanu ai!*

Afilipi 1 ndime 28 (AMP) ndi imodzi ya Mau a Mulungu a m'Bukhu Lopatulika a mphamvu kwambiri amene akupangitsa mfundo imeneyi kuti imveke bwino lomwe kwa onse. Iyo ikuti:

"Osaopa adani m'kanthu konse (ngakhale pang'ono), chimene chiri [kulimbika ndi kupanda mantha] kwa iwowa chisonyeza {chidziwitso ndi chotsindika} cha (chiri nkudza) chionongeko, koma [mphotho yosakaikitsa ndi umboni] kwa inu chipulumutso ndicho cha kwa Mulungu."

Mau a Mulungu awa a m'Buku Lopatulika akuonetseratu poyera. *Pamene mwapsyinjika, khalani mu mtendere.* Izi zimamuuza m'dyerekeziyo kwa iye ndi ogonjetsedwa. Iyeyo sadziwa zochita nanu ngati iyeyo sangathe kukuzunguzani. Imakutsimikiziraninso za kuti muomboledwa ndi Mulungu chifukwa malingaliro amenewa a mtendere ndinso mpumulo akusonyezera Mulungu kuti inuyodi mukuyendetsedwa mu chikhulupiriro cheni-cheni. Ahebri 4 akunena kuti iwo onse olowa mu mpumulo wa Mulungu akhulupirira.

Tangopitani mtsogolomo ndipo muzikasangalala ndi moyo wanu pamene Mulungu akhala akulondoloza za mavuto anu. Ine ndikukhulupirira kuti anthu ambiri ali ndi maganizo amtundu wina wake osokonekera amene amanena kuti ndikulakwitsa kumasangalala pamene ndiri ndi mavuto. Ndiponso ngati sungathe kuchita china chiri chonse, zotsatira zake ndikusautsika basi.

Ndikudziwa izi pakuti ine ndadutsamo m'maganizo a mtundu oterewu kwambiri zedi mu zaka zapitazi. Pamene mwamuna wanga ndi ine tinali pa mayesero a mtundu wina wake kapena mavuto, iyeyo amakhala wosangalala ndi kumangodzisangalatsanso iye mwini. Ine

ndimakhala wosautsidwa ndiponso kuzunguzika naye iyeyo chifukwa chakuti samafuna kuti azisautsidwa pamodzi nane.

Nthawi zambiri kulimbana kwathu kunali kwa za chuma. Mwamuna wanga amaoneka anali ndi chikhulupiriro chamtengo wapatali chapadera mu gawo la ndalama. Iye ankanena kuti, “Tipereke cha khumi komanso chopereka mowolowa manja m’mene titaonere kufunukira kwake. Baibulo likuti, *‘Ndikutaya pa Iye nkhawa yanu yonse, pakuti Iye asamalira inu.’* (Petro woyamba 5 ndime 7). Baibulo likuti, Mulungu adzakwaniritsa zosowa zanu zonse (Afilipi 4 ndime 19), ndiye ine ndidandaulirenji za izo? Kudandaula sikupangitsa kuti ndalamazo zibwere ai. Sikumatero ai.”

Iyitu inali mfundo imene mwamuna wanga “amaimapo.” Pamene Mulungu amachita nalo vuto, mwamuna wanga amangopita mtsogolo ndi kumadzisangalalira ndi moyo wake. Ine ndimati “ndikudziwa kuti mwamuna wanga sangangopanda kuchitapo kanthu kena.” Ine ndimafuna kuchitapo kanthu kena. Ndipo iyeyo amati, “Chabwino mkazi wanga, iwe ukufuna ndichitepo chiani?” Ine ndimamuuza kuti, “Upemphere! Ukuyenera upemphere.” Iye amati, “Ine ndapemphera ndipo ndamufunsa Mulungu kuti asamalire vutoli. Ndipo ine ndamafunsa Iye kuti andionetsere ine ngati pali chinthu china chiri chonse Iye akufuna kuti ndichite. Koma Iye sanandisonyezere china chiri, ndiye samachiona chifukwa chake chakuti ndizidandaulira.

Ine ndinadziwa mkati mwanga kuti mwamuna wanga amanena zoonā. Komabe, panali chinthu china chake chosokoneza chimene chimandikakamiza-kakamizabe kuti ndisakhale oyenera kumasangalala ine mwini pamene ndinali ndi vuto. Zotsatira zake zinali chimodzi-modzi kwa zaka zingapo: nthawi zonse tikakhala ndi vuto mwamuna wanga amapemphera ndipo amakhala ndi mtendere, koma ineyo ndimapemphera ndi kumadandaula. Inetu ndinadzipanga ine mwini kukhala omangodandaula. Mwamuna wanga amasangalala ndi moyo wake, ndipo Mulungu analowererapo kumapeto kwake. Nthawi zonse timagonjetsa ndithu.

Ndikuthokoza Mulungu, pomalizira pake ndinazindikira kuti palibe chomwe ndimapindulapo. Chimene ndimangochitapo pamenepo ndikumangodzipanga ine mwini kukhala omangodandaula ndiye mwina mwake ndimachedwetsa yankho lomwe limachoka kwa Mulungu kuti andipatse. Tsopanotu ndimasangalala ndi mtendere mkati mwa mafunde. (Marko 4 ndime ya 37 mpakana 40)

Yesu anati, *“M’dziko lapansi mudzakhala nacho chivuto, koma limbikani mtima; ndalilaka dziko lapansi Ine”* (Yohane 16 ndime 33B) (NKJV) Baibulo nalo likunenanso kuti kuyesedwa kukuyenera kubwera, koma tikulimbikitsidwa kuti tisalowe mu kuyesedwa. (Luka 8 ndime 13; Akoronto woyamba 10 ndime 13; Yakobo 1 ndime 12) Mfundo yanga ndi yakuti zotitsutsa, zinthu zoti tigonjetse, zidzakhhalapo nthawi zonse m’oyo uno, koma ndife oposa agonjetsi kudzera mwa Khristu Yesu. (Aroma 8 ndime 37)

Ife sitinali akuti tinagonjetsedwa ai, koma ndife agonjetsi nthawi zonse. Simudzatha kufika malo amene mwatha kugonjetsa kale zonse zotchinga, koma mungathe kukhala nacho chitsimikizo cha kupambana nthawi zonse mwa Khristu. Inu mukugonjetsa nthawi zonse!

Mudzafika pamalo pamene Paulo ananena ku Afilipi 4 ndime ya 11 ndi 12 – iye anati iye anaphunzira kukhala okwanitsidwa (mwa mtendere) kaya iye ali operewedwa kapena ochulukidwa. Ngati simutha, moyo wanu udzakhala ndi mitundu-mitundu ya zosautsa yomapita ndi kumabwera. Kumbukirani ichi: Ngati m’dyerekezi angathe kumakulondolozani ndi zinthu zokuchitikirani, iyeyo adzakudinani inu pansu pa chala chake ku nthawi zonse. Inu mutha kuyenda mu ulamuliro wanu pomakhala mu mtendere nthawi zonse.

7



KULITENGA TSIKU LIRI LONSE M'MENE LILIRI

Njira yotsindika kuti inu mukataye mtendere wanu ndikungoyambapo kumadandaula za mawa. Mateyu 6 ndime 34 (AMP) ikuti:

“Chifukwa chake musadere nkhwawa za mawa; pakuti mawa adzadzidera nkhwawa iwo wokha. Zikwanire tsiku zovuta zake.”

Ambiri mwa ife tiri ndi zokwanira zoti tizichite pa tsiku la lero posadandaulanso za mawa. Mulungu adzatipatsa chisomo chokwanira cha lero, ndipo Iye sadzatipatsa chisomo cha mawa mpakana mawalo litafika.

Nthawi zambiri anthu amangodandaula ndi kumangodandaula za chinthu china chake chomwe sichimachitikanso. Izi zomati “nanga bwanji pamenepa” ndi vutonso. Ngati mumva “nanga bwanjinso” izi kapena izo zikuyenda mu malingaliro anu, samalirani. Inu mwina mwatsala pang’ono kukokeredwera ku madandaulo tsopano. Anthu ena amadandaula kwambiri kotero kuti madandaulo awo amasunduka mantha, ndipo kawiri-kawiri zinthu zomwe anthu amakhala akuzidandaula zimabwera kwa iwo. Tikhoza kulandira kuchoka kwa Mulungu kudzera m’chisomo. Komanso tikhoza kulandira kuchoka kwa m’dyerekezi kudzera ku mantha.

Musavomere inu nokha kuti muope mawa. Ingodziwani kuti Mulungu ndi wokhulupirika. *Chiri chonse chimene mawa lasunga, Iye amasunga mawalo.* Chisomo Chake ndi chokwanira kukomana nacho chosowa chanu. Musataye nthawi kumadandaula za mawa. Ndizodabwitsiratu zedi zimene tingamapindule titamakhala tsiku liri lonse m'mene liliri.

Ine ndinaphunzira phunziro iri pamene ndinayamba kuphunzitsa ku Baibulo Koleji. Ine ndinkaphunzitsa kamodzi pa mulungu ku mpingo wathu kumene ineyo ndinalinso othandizira Abusa. Ndinali ndi ana anayi komanso ndinali pa ntchito panthawiyo m'mene unapezeka mwayi wokaphuzitsa ku Baibulo Koleji ku mpingo katatu pa mulungu uliwonse. Ine ndinalidi ndi chikhumbo chophuzitsa Mau a Mulungu kwambiri kale ndi kale, ndiye pano unapezeka mpata tsopano wophunzitsa katatu pa mulungu uli wonse.

Koma tsopano, ndikamakaphunzitsa, ndimayenerera kuwerenga kukonzekera. Makalasi ambiri anali kuphunzira Baibulo mozama ndithu, chimene chimatanthauza kufukula kwakuya m'Mau kwa ineyo kuti ndikhale wokonzekera, maka-maka chaka choyamba. Kuwerenga konseko kumayenera kupangike madzulo, chifukwa chakuti ntchito yanga inali ya nthawi ya masana. Ine sindinathe kuziona m'mene ndikanathera kuzichita zimenezo, koma ndimamva kuti Mulungu amafuna kuti ine ndithe.

Nditapemphera ndi kulingaliranso kwambiri, ndinatuluka kwa Mulungu ndikukupanga chosathekera mwa Iye. Chinthu chachikulu chimene Mulungu anapitiriza ku chikakamiza pa ine: “Tsiku liri lonse m'mene liliri, ndipotu iweyo ungate kuchichita ichi.” Ngati ndikanayamba kuganiza za mawa, ine ndikanakhala m'mavuto akulu zedi mwansanga-nsanganso chifukwa nthawi yomweyo ndikanaona zosatheka. Komatu, tsiku liri lonse m'mene liliri, zonse zinatheka ndithu. Mulungu anandipatsa chisomo, koma sanatero mpakana tsiku limene ndinachifunitsitsa icho. Chaka cha chiwiri chake zinali zosavuta kweni-kweni chifukwa tsopano ndinali ndi zonse zoyenereka kukaphunzitsa. Choncho, sindinafunikire kumakawerenga kwambiri

ngati m'mene zinaliri mu chaka choyamba.

Panali zifukwa ziwiri zofunikira zedi Ambuyeyo anandifunsa kuti ndithane nazo zimenezi, pambali pophuzitsa ana asukulu Mau a Mulungu. Choyamba chinali kukhala kukumana nako kweni-kweni kwa mulingo waphindu la zimene chisomo cha mwa Mulungu ngati moyo ungatengedwe tsiku liri lonse m'mene liliri. Chinanso kunali kuti ndikhale ndi kuzama kophunzitsa kwa pafupi-pafupi choncho. Inetu panopa ndimaphunzitsa pafupi-pafupi pamene mwamuna wanga ndi ineyo timayenda-yenda ndikumaphunzitsa kuphatikiza kuchita ndondomeko ya misonkhano ya "Life In The Word" kunyumba. Mulungu ndi wabwino, ndipo Iye njira zake ndi zolungama.

Gawo lina limene lirinsu mu m'ndandanda womwewu umene umawapangitsa anthu kugwa m'mavuto ambiri ndi kudzimvera chisoni – kumakhala modzimvera chisoni pa zinthu za dzulo. Tonse timalakwitsa! Ngakhale iwo amene amaganiza kuti sapanga chiri chonse cholakwika amalakwitsa. Baibulotu limati tonse tiri ndi kaphukusi kathu kakang'ono ndithu ka zolakwika zotipsyinja. (Agalatiya 6 Ndime 5) Tonse timayankhula zinthu zimene sitikanafuna titazinena kapenanso kuzichita. Koma chinthu chikachitika, chachitika.

Ine ndaphunzira kuti kusiyana ndi kuutaya mtendere wanga pa chinthu china chake chimene ineyo ndachita koma sindingathe kuchitapo chiri chonse pa icho panopa, ine ndingokhulupirira Mulungu kuti achipangitse icho kuti chiyende bwino. Iye amayeretsa zolakwa zanthu.

Nthawi zina ndimanena china chake chimene ndikanakondwera ndikanapanda kuchinena. M'malo momadandaula kuti kapena mwina ndamulakwira wina wake kapenanso kuwazunguza ndi zimenezo, ine ndimamupempha Mulungu kuti awazindikiritse kuti mtima wanga unalibe mangawa, ngakhale ndinaika phazi langa mkamwa mwanga. Ine ndimamukhulupirira Iye kuti agwira ntchito mu mitima yawo ndi kundipatsa ine zokoma. Munjira imeneyo sinditha masiku angapo ndikudandaula, ndi kubisala ndikawaona iwo.

Timagwa m'khwekhwe lodzimvera chisoni pa zinthu zambiri-mbiri. Ine ndi mwamuna wanga nthawi zambiri timakadya kumalo ogulitsako zakudya zophika-phika chifukwa chakutanganidwa kwathu. Munthawi zina, timakadya kumalo komwe chakudya chake sichikhala chabwino ai, kapenanso kalandiridwe ka alendo ndikoipa. Timapezeka kuti ife timangochokako kumeneko, kenaka kumadzimvera chisoni pakapita maola angapo kuti tinapita kumalo oterowo. Ambuyetu anatisonyeza kuti angakhale kudzimvera chisoni pa kusankha kosayenerera kwa ku malo okadya kungathe kutibera mtendere wathu.

Kumbukirani, kuti musangalale ndi mtendere, siyani kumayesera kuchita china chake pa zinthu zomwe inu simungathe ai konse kuchitapo chiri chonse. Pamene mwafika pa malo ena ake ndikuchita za ntchito za malonda ndi kugula ndipo mwalipira, kudzimvera chisoni sikungasinthe zimene zachitikazo.

Tsopano tikhoza kutembenuza zinthu zochitika ngati zimenezo ndi kuzipanga kuti zitichitire ubwino. Tsopano tinganene kuti “Tangoganizirani anthu onse amene angapite kumalo kumenekoko ndikusakakhutitsidwa. Pamapeto kodi ifeyo siodalitsika! Kuti tatha kuzindikiriratu mwansanga kuti sikumalo kodzapitakonso ai. Sitidzakatayakonso nthawi ndi ndalama zathu popita kumenekonso.

Ndiri ndi chopachika pakhoma la m'nyumba mwanga chimene chinalembedwapo zinthu zotere: Mukayesera kukhala masiku apitawo, moyo udzakhala olimba. Yesu sananene kuti Iye ndi opambana “Ine ndinali.” Mukayesera kukhala moyo wa mtsogolo, moyo udzakhala olimbanso. Yesu sananene kuti iye ndiopambana ai “Ndidzakhala.” Inu mukalitenga tsiku liri lonse m'mene liri kubwerera, moyo wanu udzayenda bwino. Yesu anati, “Ine Ndiri” (Yohane 8 ndime 58) Iye ali ndi inuyo nthawi zonse mu chinthu chiri chonse chomwe mukudutsamo panthawi ino. Mutangokumbukira kumudalira Iye pa chisomo chokwanira pa tsiku la leroli basi.

8



PEMPHEREO LIMADZETSA MTENDERE

Afilipi 4 ndime 6 ikuti:

“Musadere nkhawa konse” (musakhumudwe ai); “komatu mu zonse ndi pemphero ndi pembedzero, pamodzi ndi chiyamiko, zopempha zanu zidziwike kwa Mulungu.”

“Ndipo mtendere wa Mulungu wakupambana chidziwitso chonse, udzasunga mitima yanu ndi maganizo anu mwa Khristu Yesu.”

Mtendere umenewu womwe umapambana chidziwitso ndi chinthu cha mtengo wapatali kuwudutsamo. Momwe zinthu zili kukhalira, muyenera kuzunguzika, kupanikizika, kukhala mu chipwirikiti ndi kudandaula, koma inu muli ndi mtendere umene uli osaneneka, ndi chinthu chamtengo wapatali kudutsamo. Dzikolitu liku ulaka-laka mtendere wa mtundu umenewu. Simungathe kuugula; chifukwa siugulitsidwa ai. Iwo ndi mphatso yaulere yochoka kwa Yesu. Ndi yanu ndithu mukangomulandira Iye ngati Mbuye ndi mpulumutsi wanu ndi kuphunzira kuchita zofuna za Iye mwini.

Pemphero loikika ndi pemphero la mphamvu limene limachotsa nkhawa zanu kwa inuyo ndikuzipititsa kwa Yesu. Petro Oyamba 5 ndime 7 ikuti, *“Ndi kutaya pa Iye nkhawa yanu yonse, pakuti Iye*

asamalira inu.” Ma Baibulo ena amatathauzira pa 1 Petro 5 ndime 7 Baibulo la Amplified limatathauzira kuti:

“Kutaya nkhawa yanu yonse yanthuthu[zothodwa zonse, madandaulo onse, zokukhudzani zonse, koyamba ndi kumapeto pa Iye, pakuti Iye amasamalira inuyo ndi chikondi cheni-cheni ndi kusamalira za inuyo molondolozeratudi.”

Chinthu cha mtengo wapatali bwanji! Akhristu ambiri sagwiritsa ntchito yaikulu mphatso yapaderayi ngakhale iyoyi iri ya iwowo eni ake.

Kodi mukusangalala ndi mtendere umene umabwera chifukwa chakuti mwataya nkhawa zanu pa Iye? Liu loti kutaya limatanthauza kuti kuponya kapena kugenda kwa mphamvube. Inu mukachichita ichi mwachangu ndi bwino ndithu. Muchichite ichi kudzera mu pemphero. Muikize vuto lanu mu chisamaliro chake cha chikondi. Muchite ichi mwachangu panthawi yomwe Mzimu Oyera utango kuzindikiritsani kuti inuyo mukudandaula kapena kuti mwautaya mtendere wanu.

Satana akufunatu kuti inu muzingodandaula. Petro oyamba 5 ndime 9 (AMP) ikuti ku “mumukanize” m’dyerekeziyo “mu zotchera zakezo” – kutanthauza kuti poyamba pomwepo pa chipseyinjo panthawi yomweyo basi. Musayembekezere konse mpakana pamene iyeyo wapeza mpata kuti agwire nchito kotheratu pa inu kwa masiku angapo. Pamene mukudikira kwa nthawi yaitali, ndi pamene m’dyerekeziyo amakhwimitsa kugwidwa kwake kwamphamvu pa inuyo. Tsopano zimakhala zovuta kuti mumasulidwe kuchokamo m’menemo. Pamene mwangozindikira inuyo kuti mukudandaula, mukane kudandaulako. Tayani chisamaliro cha zochitikazi pa Mulungu. *Sinthani njira yomwe inu mumaganizirira.*

Poyamba m’mene ndinkaphunzira kufunikira kwa “kutaya chisamaliro changa” ndinso “kusadandaula.” Ndinkadziwa kuti maganizidwe anga anali olakwika. Ndimatha tsiku lonse ndi kumatayira malingaliro ena ndi ena, kenaka amangobwera-bweranso

kwa ineyo mwini wake. Ndikukumbukira nditavutika zedi ndi chinthu chimenechi. Ine ndinati kwa Ambuye, “Kodi munthu angathe bwanji kutha osaganizira za chinthu china chake?” Inu mukuona pamenepa, kuti usamakadandaule, usamaliganizire vutolo. Pamene ukufuna kuchiganizira ichocho kuti upange mfundo zofunikira, ukuyenera kuchiganizira mwa chiyembekezo osati motsutsana ai. Iwe ukhale nalo vuto lakolo chiyembekezo cheni-cheni osati kutsutsana nalo ai.

Ine ndikukumbukira bwino lomwe zimene Yesu ananena kwa ine pamene ndinafunsa, “Zingatheke bwanji kuti ine ndisathe kumaliganizira vuto limeneli?” Iye anati, “Ndizosavuta ngakhale pang’onotu iwe, Joyce. Uzingoganizira za zinthu zina ndi zina.” Inu mukuona pamenepa, inu simungathe kuliganizira vutolo ngati inu mukuganizira za zinthu zina zomwe siziri vuto.

Afilipi 4 ndime 6 ikuti musadandaule koma m’ malo mwake pempherani. Ndime 7 ikulonjeza kuti ngati muchita za pa ndime ya 6, inu mudzakhala ndi mtendere umene umapambana chidziwitso chonse. Ndime 8 (AMP) ikuti:

“Chotsatira abale, zinthu ziri zoona, ziri zolemekezeka, ziri zonse zolungama, ziri zonse zoyera, ziri zonse zokongola, ziri zonse zimveka zokoma, ngati kuli chokoma mtima china, kapena chitamando china, zilingalireni...izi...”

Tsopano ndi pemphero langa kuti Mulungu akupatseni inu chisomo, chimene chiri mphamvu ya Mzimu Oyera, kuti muziike zinthu zofunikira kuti zigwiredi ntchito miyoyo yanu kutitu musangalale ndi m’ dalitso wamoyo wa mtendere. Ndikupempheranso kuti Atate athe kukhala ndi chiyambi chomasuka kukugwiritsani inu ntchito mu kulemekezeka ndi ulemerero Wake.

PEMPHERO LA CHIPULUMUTSO



Mulungu amakukondanani ndipo akufuna kuti kukhale pa ubale wabwino. Ngati simunamulandire Yesu ngati mpulumutsi, mukhoza kumulandira tsopano. Tsekulani mtima wanu kwa Yesu ndi kupemphera pemphero ili....

“Atate ndikudziwa ndakuchimwirani, mundikhululukire. Ndisambitseni. Ndikulonjeza kukhulupilira Yesu mwana wanu. Ndikukhulupilira anandifera – ananyamula machimo anga pamene anafa pa mtanda. Ndikukhulupilira kuti anauka kwa akufa ndipo ndikupereka moyo wanga kwa iye tsopano.

Zikomo atate chifukwa cha mphatso ya chikhulukiro ndi moyo wosatha. Ndithandizeni kukhala moyo wa inu mdzina la Yesu, Amen”.

Monga momwe mwapempera mu mtima mwanu, Mulungu wakulandirani, wakuyetsani ndikumasilani ku ndende ya imfa ya uzimu. Pezani nthawi ndikuwerenga mawu awa ndikufunsa Mulungu akulankhuleni pamene mukuyenda naye mmoyo watsopanowu.

Yohane 3:16

1 Akorinto 15:3-4

Ayefeso 1:4

Ayefeso 2: 8-9

1 Yohane 1:9

1 Yohane 4:14-15

1 Yohane 5:1

1 Yohane 5:12-13

Pempherani kuti Yesu akuthandizeni kupeza mpingo wophunzitsa ndi kukhulupilira Baibulo kuti mulimbikitsidwe ndikukula muchiyanjano ndi Yesu Christu. Mulungu alinanu nthawi zonse akutsogolerani tsiku ndi tsiku ndipo akuwonetsani mmene mmene mukhalire mmoyo watsopano!

ZA OLEMBA BUKHULI



Mai JOYCE MEYER wakhala akuphunzitsa za Mau a Mulungu kuyambirachaka cha 1976 ndinso muutumiki wamphumphukuyambira chaka cha 1980. Iyeyu ndi munthu amene mabuku ake agulitsidwa kwa mtengo wa patali kwambiri pa mabuku oposeru makumi asanu ndi mphambu zinayi, kuphatikizirapo mabuku awa; *Secrets to Exceptional Living* (Zinsinsi za Chikhalidwe cha Padera), *The Joy of Believing Prayer* (Chimwemwe cha Pemphero la Chikhulupiriro) ndi *Battlefield of the Mind* (Bwalo la nkondo la m'malingaliro), pamodzinso ndi ma alabamu a makaseti omvetsera oposeru mazana awiri ndi mphambu makumi awiri ndinso a vidiyo okwanira makumu asanu ndi anayi. Mapologalamu amayi Joyce otchedwa *Life in the Word* (Moyo wa m'mawu) ndi mapologalamu apa tivii amaulutsidwa kuzungulira dziko lonse la pansu, ndipo amayi Joyce amayenda kwambiri kugawana maulaliki ake mu misonkhano yotchuka zedi ya "Life in the Word" (Moyo wa m'mawu). Mayiyu Joyce ndi abambo akunyumba kwawo a Dave ali ndi ana anayi ndipo amakhala ku St. Louis, ku Missouri.